



MUTU 4:

*EKSODO*

---



ANAYENDA MPAKA KUPYOLA MAPIRI NAKAFIKA  
PAFUPI NDI NYANJA YOFIIRA. KUMENeko  
ANAMANGA MSASA NAMAKAMBIRANA ZA MMENE  
ANGAOLOKERE NYANJA YA MADZI AMBIRIYO.

ATATHA KULIRA MWANA WAKE,  
FARAO ANAKWIYA KWAMBIRI KUPOSA  
KALE. NCHIFUKWA CHIYANI ADALOLA  
KUTI AKAPOLO AKE AMUKE?




KONZANI MAGARETA.  
LONDOLANI AHEBRI.  
MUWAPHE ONSEWO,  
KAPENA MUBWERERE  
NAWO KUNO.

TIDZACHITA  
MONGA  
MWANENERA,  
MFUMU.



**ONANI, GULU  
LANKHONDO LA  
AIGUPTO LIKUBWERA!  
TITHERA M'CHIPULULU  
MOMWE MUNO  
BASI!**


**MOSE ANATIBWERETSA  
KUNO KUTI TIDZAFE. KUNALI  
BWINO KUTI TIZIKHALA NGATI  
AKAPOLO KOMWE KUJA  
M'MALO MODZAFERA M'MALO  
ACHABECHABEWA.**



TAZUNGULIRIDWA  
NDI MAPIRI NDIPO  
NYANJA ILI PAFUPI  
NAFE. TAKODWA  
BASI.

TSOPANO  
PALIBE CHIMENE  
MULLINGU  
ANGACHITE KUTI  
ATIPULLUMUTSE.

PAMENE AIGUPTO ANAONA  
AHEBRI OPANDA MPHAMVUWO,  
NAKUMBUKIRA MAVUTO ONSE  
AMENE MOSE ANADZETSA KWA  
AIGUPTO, ANAKONZEKA ZEDI  
ZOPHA AHEBRIWO.




IMANI POMWE  
MULIPO. MULINGU  
ATIPULUMUTSA  
MWAMPHAMVU  
ZEDI.

MULINGU WAUMITSANSO  
MTIMA WA FARAO.  
KUYAMBIRA LERO MPAKA  
MUYAYA SIMUDZAWAONANSO  
ASILIKALI A AIGUPTO.


EKSODO 14:5-13



PAMENE ZINKAONEKA KUTI ANKHONDO A AIGUPTO ATSALA PANG'ONO KUTHIRA NKHONDO AHEBRI, MOTO WAIKULU WOCHOKERA KUMWAMBA UNAWATSEKERA NJIRA. PA USIKU UMENEWO, AHEBRI ANALI M'KUWALA KOMA AIGUPTO ANALI MU MDIMA.



MOSE ANALOZA NDODO YAKE  
KU NYANJA NDIPO MPHEPO  
YAIKULU INADZA KUCHOKERA  
KUMWAMBA, INAOMBA  
PANYANJAPO, NYANJAYO  
NKUGAWIKANA, NJIRA YOLIMA  
INAONEKA M'KATI MWA  
NYANJAMO, PANSI PENIPENI  
PA NYANJAYO.



CHOZIZWITSA CHIMENECHI  
CHINALI CHACHIKULU.  
AISRAELE ANAOLOKA  
NYANJAYO POLIMA.

PAMBUYO PAKE ANKAIMBA ZA  
MULLINGU AMENE ANAKONZA NJIRA  
PA NYANJA. ANTHU ONSE ADAADZIWA  
KUTI KULI MULLINGU MMODZI YEKHA  
WOTCHEDWA YEHOVA.





ICHI CHAPAMBANA  
ZIMENE  
TIDAAWONA KU  
EJIPITO.

EEEE, MULLINGU  
WATHU NDI MULLINGU  
WABWINO KUPOSA  
MILLINGU INA YONSE!  
TILI M'KATI MWA  
NYANJA.



**YOSIYA! KODI  
NDIWE WAMISALA?  
CHOKA PAMENEPO!  
SLINGASAMBIRE!**



NDINGOFUNA  
NDIGWIRE NSOMBA  
YOKONGOLAYI.

PAMENE AHEBRI ANALI  
PAFUPI KUOLOKA,  
MULLINGU ANACHOTSA  
KHOMA LA MOTO LIMENE  
LIDAATSEKEREZA  
AIGUPTO. AIGUPTOWO  
SANAONE MMENE  
NYANJA IDAGAWIKIRA,  
CHONCHO ADAYAMBA  
KUTSOTSOMBETSA  
AHEBRI AJA.

**TIYENI,  
IPHANI  
AHEBRIWO!**




**EKSODO 14:22-23**




**LERO MWAONA  
MPHAMVU ZA  
YEHOVA.**

**ONANI, MADZI  
AJA AKUBWERERA  
M'CHIMAKE. AMIZA  
ANTHU ONSEWO.**



ASILIKALI ONSE A IGUPTO  
ANAMIRA M'NYANJA. MILLINGU  
YAO YA MITENGO NDI MIYALA  
SIDAWAPULLUMUTSE.

EKSODO 14:27-28



TAONANI  
MITEMBOYO.  
NYANJA YADZAZA  
NDI MITEMBO YA  
ASILIKALI A  
AIGUPTO.

ZOONADI, YEHOVA  
YEKHA NDI AMBUYE.  
PALIBE WINA AMENE  
ANGACHITE ZIMENEZI.  
TSIKULI TIDZALIKUMBUKIRA  
MPAKA KALEKALE.



ATACHOKA KU NYANJA YOFIIRA KUJA,  
ATASIYA MITEMBO YA ASILIKALI A IGUPTO  
M'NYANJAMO, AHEBRI ADALONDOLA MOSE  
NDI MTAMBO MPAKA ANAFIKA M'CHIPULULU  
CHACHIKULLI. ANKADYA NDI KUMWABE  
ZIMENE ADAACHOKA NAZO KU IGUPTO.

ATAYENDA ULENDU WAO KWA MASIKU AMBIRI,  
MTAMBO UMENE LINKAWATSOGOLERA UNAIMA PA  
ZITSIME ZA MADZI. AHEBRI ANAMANGA MISASA  
PAMENEPO MPAKA CHAKUDYA CHAO CHIJA  
CHINATHA. KUNALIBE KWINA KOKAPEZA CHAKUDYA  
CHINA. CHIYEMBEKEZO CHAO CHINAYAMBA KUZILALA.



KUNALI BWINO TIKANAKHALA  
KU IGUPTO KUSIYANA NDI  
MMENE TIKUKHALIRA  
M'CHIPULULU MUNO. MONGA  
AKAPOLO, CHAKUDYA CHATHU  
CHINKATIKWANA. KUNO  
KULIBE CHILICHONSE.



INDE, KODI  
UNATIBWERETSA  
KUNO KUTI TIFE  
NDI NJALA?



TANDIMVERANI. INU  
SIMUKUDANDAULIRA  
INE, KOMA  
MULINGU AMENE  
TIMAMUKHULLUPIRIRA.

YHOVA AKUTI ADZAGWETSA  
MKATE KUCHOKA KUMWAMBA. MMAWA  
ULIWONSE MUZIKAUPEZA UTAYALA  
PANSI. MUZIDZANGOWUTOLA,  
NKUMADYA.



KODI MOSE ANATI  
CHIYANI? CHAKUDYA  
TICHIPEZA BWANJI? ANA  
AKUNYENTCHERA.

AKUTI YEHOVA...  
AZIGWETSA MKATE MMAWA  
ULIWONSE KUCHOKERA  
KUMWAMBA.



PANOPA DZUWA LAKHALA  
PANG'ONO KUTULUKA. KODI  
MUKUKHULLUPIRIRA KUTI TIKAPEZA  
MKATE UTAGWA PANSI MONGA  
MOSE ANANENERA?

TINYENTCHERA  
NGATI  
SITIKALUPEZA.

KODI MUDAMVAPO  
ZA MKATE  
WOGWA KUCHOKERA  
KUMWAMBA.

AI, KOMA SINDINAMVEPONSO  
ZA NJIRA YOUMA M'NYANJA. MULLINGU  
WA MOSEYU AYENERA KUTI NDI MLENGI  
WA DZIKO LAPANSI NDI KUMWAMBA.  
NDIGANIZA KUTI SICHOVUTA KUTI AGWETSE  
MKATE KUCHOKERA KUMWAMBA. TIYENI,  
NTHAWI IJA YAKWANA. TIYENI  
TIPITE TIKAOONE.



MKATE  
WOCHOKA  
KUMWAMBA,  
MONGA MUJA  
ANANENERA.

NCHIFUKWA  
CHIYANI  
NTHAWI ZONSE  
TIMAKAYIKA?



**ONANI!** ULI  
PONSEPONSE.

EEEE NDI  
WOKOMA!  
LUKUKOMA  
NGATI UCHI.

ZOONADI, YEHOVA NDI  
MULLINGU NDIPO MOSE  
NDI MNENERI WAKE.

NTHAWI YONSE  
IMENE ANALI  
M'CHIPULULU,  
MULINGU  
ANKAWADYETSA  
CHAKUDYA  
CHAKUMWAMBA  
CHA ANGELO,  
CHOTCHEDWA  
'MANA.' 'MANA' NDI  
MAU ACHIHEBRI,  
KUTANTHAUZA  
"ICHI NCHIYANI?"



NTHAWI ZONSE MTAMBO UKAIMA PA MSASA  
WAO, AHEBRI ANKAKHALA PAFUPI NDI MITSINJE  
YA MADZI NKUMADYA MKATE, KOMA  
MTAMBOWO UKAYAMBA KUYENDA,  
ANKALONGEZA MAHEMA AO NKUMAILLONDOLA  
MPAKA KU CHIPULULU CHOSADZIWIKA.




KOMA NTHAWI  
INAFIKA PAMENE  
MADZI ANASOWA.

CHONCHO  
ANATIPATSA  
MKATE, KOMA  
TSOPANO  
AFUNA KUTIPHA  
NDI LUDZU.

MWANA WANGA  
AMWALIRA NGATI  
SITIFEZA MADZI  
MSANGA.








TIKADANGOKHALA KUJA KU  
IGUPTO. TSIKU LINA ZIWETO ZATHU  
ZONSE ZIDZAFI, PAMBUYO PAKE ANA  
ATHU NAWONSO ADZAYAMBA KUIFA.  
TIPHWANYA MUTU WAKOWO  
NDI MIYALA.

KODI MULLINGU  
ALI NAFE  
KAPENA AI?

NDIPITA  
KUKAYANKHU  
LA NDI  
YHOVA.

EKSODO 16:14-15, 17:2-4;  
MASALIMO 78:24-25



MULUNGU  
ADALIZA MOSE  
ZOTI ACHITE.

BWERANI TIDZAONE MPHAMVU  
ZA YEHOVA. SIMUMUKHULLUPIRIRA.  
MUMANGONYONG'ONYEKA NDI  
KUMANGODANDAULA.

ANAKUPATSANI MKATE,  
NDIPO TSOPANO AKUPATSANI  
MADZI KUCHOKERA M'MWALA  
WOLIMAWU.





**AAAAAAA!**

**EEEEEE!**

**EKSODO 17:5-6**

MADZI ANAYENDA  
NGATI MTSINJE.






MTAMBO UNAYENDANSO, NDIPO  
AHEBRI ANALONGEZA KATUNDU WAO  
NKUMAILLONDOLA M'CHIPULULLUMO  
KUPITA KU PHIRI LOTCHEDWA SINAI.

KUMENEKO MOSE ANAPEMPHERA,  
NDIPO MULLINGU  
ANAYANKHULANSO NDI MOSEYO.

**LWAKUMBUTSE ZIMENE  
NDINACHITIRA AIGUPTO, MMENE  
NDINAWAPULLUMUTSIRA, MMENE  
NDINKAWADYETSERA, NDI  
MMENE NDINAWAPATSIRA  
MADZI KUCHOKERA M'MWALA.**




A man with a beard, wearing a dark tunic, stands in the foreground looking towards a vast camp of many small, conical tents. The camp is situated in a valley with mountains in the background under a sky with soft, colorful clouds. The scene is rendered in a stylized, illustrative manner.

**LIWALUZE KUTI  
AKAMVERA MALAMULO  
ANGA, ADZAKHALA ANTHU  
ANGA OPATULIKA PAKATI PA  
MITUNDU YONSE YA ANTHU A  
PA DZIKO LAPANSI.  
AKAMVERA, ADZAKHALA  
ANTHU ONDITUMIKIRA  
NGATI ANSEMBE.**

**MOSE, NDIKAMAYANKHULA  
NDI IWE, NDIZIBWERA MU  
MTAMBO WOLEMERA KUTI  
ANTHU ATHE KUONA, KUMVA  
NDI KUZINDIKIRA KUTI  
NDINE.**





MOSE ANATSIKA  
PHIRI LIJA NAUZA  
ANTHU ZONSE  
ZIMENE MULLINGU  
ANANENA.

TIDZAMVERA.  
TIDZACHITA ZONSE  
ZIMENE MULLINGU  
WANENA.

NDIYETU TSONO PITANI,  
KACHAPENI ZOVALA ZANU  
NDIPO MUKASAMBITSENSO  
MATUPI ANU; KONZEKERANI  
KUPEMBEDZA MULLINGU.  
PATAPITA MASIKU ATATU  
KUCHOKERA LERO, MULLINGU  
ADZAKUYENDERANI.

MONGA MULINGU ANALAMULIRA,  
PA TSIKU LACHITATU ANTHU  
ANASONKHANA PAFUPI NDI PHIRI  
LIJA KUDIKIRA KUTI MULINGUYO  
AWAYANKHULE. MTAMBO WODABWITSA  
UNADZA PAPHIRIPO NDIPO...



*MOSE, BWERA  
PAPHIRI PANO.*

A comic book illustration of Moses standing on a rocky ledge. He is wearing a blue tunic and a yellow sash. His arms are raised, and he is looking upwards. Behind him is a bright, glowing light that illuminates the scene. The background is a dark, swirling pattern.

**MOSE, INE NDINE  
YEHOVA MULLUNGU, AMENE  
NDINATULUTSA INU M'DZIKO  
LA IGUPTO. UKATSIKA,  
UTCHINGIRE PHIRI LONSE.**

**WINA ALIYENSE  
AKAKHUDZA PHIRI  
LIMENELI ADZAFI.  
NDIKUPATSA MALAMULO  
KHUMI AMENE LYENERA  
KUKAWAUZA ANTHU  
PANSIPO.**



MUSAKHALE NDI MILINGU INA  
KOMA INE NDEKHA.

MUSAPANGE FANO LA MTUNDU  
WINA ULIWONSE NDIPO  
MUSALIGWIRITSE NTCHITO  
NGATI CHIDA  
CHOKUTHANDIZANI  
POPEMBEDZA.

OSATCHULA DZINA LANGA  
MOSAKHULUPIRIKA NDI  
MWACHIBWANA.

OSATCHULA DZINA LANGA  
MOSAKHULUPIRIKA NDI  
MWACHIBWANA.

LEMEKEZANI ATATE ANU NDI  
AMAI ANU.


MUSAPHE.

MUSACHITE CHIGOLOLO.

MUSABE.

MUSANAMIZIRE ANZANU.

MUSAMASIRIRE ZINTHU ZA  
ANZANU.



MOSE ATATSIKA PHIRILO,  
ANAITANA ATSOGOLERI 70  
A AISRAELE NAWAUZA ZA  
MALAMULO KHUMI A  
MULLINGU.


TIDZAWATS  
ATIRA.

NDI  
MALAMULO  
ABWINO.

INU ANTHU 70  
MUBWERERE NDI INE KU PHIRI.  
MULLINGU ADZAKUMANA NANU  
KUMENECO MONGA ANACHITIRA NDI  
INE. MUKADZIONERE NOKHA, PAJA  
ZAKUMVA ZIMAPWETEKETSA MUTU.  
KOMA POYAMBA NDIYENERA KULEMBA  
M'BUKU MALAMULO AMENE  
MULLINGU ANANDIIZA.

MOSE ANAYENERA KULEMBA  
MOSAMALA ZONSE ZIMENE  
MULLINGU ANAYANKHULA. MZIMU  
WA MULLINGU ANAMUTHANDIZA  
KUTI ASAPHOPHONYEPO KANTHU.



A man with a beard and curly hair, wearing a yellow robe, stands on the left side of the frame. He is holding a large scroll and looking towards a large crowd of people on the right. The crowd consists of many individuals, mostly men, wearing head coverings and simple clothing. The background is a plain, light-colored wall.

MOSE ATATHA KULEMBA  
MALIWO,  
ANASONKHANITSA ANTHU  
ONSE PAMODZI  
NAWAWERENGERA MALI A  
MULLINGU AJA.

ZONSE ZIMENE  
MULLINGU  
WANENA NDI  
ZABWINO, NDIPO  
TIDZAZIMVERA.

CHONCHO FUKO LA ISRAELE  
LINACHITA PANGANO NDI MULLINGU.  
MULLINGUYO ADALONJEZA  
KUWADALITSA, KUWAPATSA MOYO,  
NDI KUWATETEZA KWA ADANI AO,  
NDIPO IWO ANALONJEZA KUTI  
ADZAMVERA MALAMULO ONSEWO,  
NDIPO KUTI ADZACHITA CHILINGAMO.

MULUNGU ANALAMULA MOSE KUTI  
APERKE NSEMBE YAMAGAZI NDI  
KUWAZA ANTHU MAGAZIWO.







ONSE ANALI OCHIMWA, OYENERA  
KUFA NDITHU, KUPHATIKIZAPO MOSE NDI AARONI. KOMA  
MULLINGU ANAWACHITIRA CHIFUNDO. ANAKONZA NJIRA  
YOWAPULLUMUTSIRA. POPHA MWANAWANKHOSA WOSALAKWA  
NDI KUWAZA FUKOLO MAGAZI, MULLINGU ANAPHIMBA MACHIMO  
AO NDIPO SANAWAPHE NGAKHALE ANALI OYENERA KUFA.  
MWANAWANKHOSA AMENE SANAYENERA KUFA NDIYE ANAFA  
M'MALO MWA ANTHU OCHIMWA AMBIRI AMENE ANAYENERA KUFA.



TSOPANO POPEZA MACHIMO ANU AKHULLULUKIDWA, INU ANTHU 70 MUPITA NDI INE PAMWAMBA PA PHIRILO NDIPO MUKAONA ULEMERERO WA MULLINGU.




CHONCHO ATSOGOLERI 70 A  
AISRAELE ANAPITIRA LIMODZI  
NDI MOSE KU PHIRI KUJA  
KUMENE MULUNGU  
ANAYANKHULA NDI MOSE.

**MWADZIDZIDZI, ANAONA  
MPANDO WACHIFUMU WA  
MULLINGU PATSOGOLO PAO.**



**ULEMERER  
O WA  
MULLINGU!**



**ATSOGOLERI 70 AJA  
ANAONA MOSE AKUPITA  
M'PHIRIMO NDIPO ANABISIKA  
M'KUWALA KWA ULEMERERO  
WA MULLINGU.**

**KUKONGOLA  
KWAKEKO!**

**KOMANSO  
ULEMERERO.**


**PALIBE MUNTHU  
WOFANANA NDI MOSE  
AMENE AMAYANKHULA  
NDI MULLINGU MASO  
NDI MASO.**

**MOSE, UMANGE HEMA  
LOPATULIKA MMENE  
MUZIDZANDIPEMBEDZERAMO.  
LIKHALE NDI GUWA LA NSEMBE  
PAMENE MUZIDZAPEREKERAPO  
NSEMBE, NDI MALO OPATULIKA  
KUMENE NDIZIDZAKUMANA NDI  
MKULU WA ANSEMBE KAMODZI  
PA CHAKA CHILICHONSE PA  
MIBADWO YANU YONSE.**



**NDIKULUZA MWATSATANETSATANE  
MMENE UDZAKONZERE HEMALO.  
M'FUKO LA ALEVI NDIMO  
MUDZACHOKERA ANSEMBE ANGA,  
NDIPO AARONI, NDI ANA AKE  
AAMLUNA, PAMBLYO PAKE NDIWO  
ADZAKHALA AKULU A ANSEMBE.  
AZIDZAPHUNZITSA ANTHU KUTI  
AKHALE OLUNGAMA NDIPONSO  
AZIDZAPEREKERA NSEMBE  
ANTHU AKACHIMWA.**





PAPITA MASABATA  
ANGAPO TSOPANO  
CHIBISIKIRE NDI MOTO  
M'PHIRIMO. AYENERA KUTI  
ANAFA TSOPANO.

SITINGAKHALE  
M'CHIPULULU  
MUNO MPAKA  
KALEKALE.

TIYENERA KUTI  
TIPEZE MULLINGU WOTI  
ATITSOGOLERE MONGA  
MOMWE MOSE  
ANKACHITIRA.

TIYENI  
TIPANGE FANO  
LAGOLIDE KUTI  
LIKHALE  
MULLINGU  
WATHU.





MOSE  
WAMWALIRA.  
AARONI  
ADZATIPANGIRA  
MULINGU  
WAGOLIDE WOTI  
ATITSOGOLERE  
KUBWERERA KU  
IGUPTO.

PATSENI  
GOLIDE  
WANU.

NDI MANJA AO, ANTHU OPLUSAWO ANAPANGA FANO LA NG'OMBE YAIMUNA NALITCHA KUTI MULLINGU. CHIFANIFANI CHA SATANA ASANACHIMWE CHINALI CHA NG'OMBE YAIMUNA. NGAKHALE ANTHUWO SANKAZINDIKIRA, SATANA ANAWALOWA M'MAGANIZO MWAO KUTI AMUPEMBEDZE.



AARONI ANACHITA MONGA MOMWE ANTHUWO ANAFUNIRA, NDIPO ANAWATHANDIZA KUPANGA NG'OMBE YAMPHONGO YAGOLIDE.

EKSODO 20:4, 25:8-9, 28:1-3, 28:1-4; EZEKIELE 1:10, 10:11, 28:14



LIYU NDI MULLINGU WANU  
AMENE ANAKUTULUTSANI M'DZIKO  
LA IGUPTO. MAWA TIDZALENGEZA  
MSEMBE YAIKULU NDIPO  
TIDZAPEMBEDZA YEHOVA.

AARONI ANACHITA MOPUSA.  
ANKADZIWA KUTI FANOLO  
SILINALI MULLINGU, KOMA  
ANKAOPA ANTHU AJA.

MULUNGU ANALI  
ATAWACHENJEZA  
KALE KUTI  
SAYENERA KUPANGA  
FANO LILILONSE  
KUTI LIWATHANDIZE  
POPEMBEDZA, KOMA  
ANKANGOTSATIRA  
MAGANIZO AO.



ANTHU AJA ANAVINA MPAKA KUKHALA  
MALISECHE. ANALEDZERA NDIPONSO  
ANACHITA CHIGOLOLO. MULUNGU  
ANAKONZA ZONONGA ANTHU ONSEWO  
NDI KUWAPONYA KU MOTO UMENE  
ANAKONZERA SATANA NDI ANGELO AKE.



**MULLINGU ANAYANKHULA NDI MOSE  
NATI, "TSIKA TSOPANO. ANTHU ACHITA  
TCHIMO LALIKULU. AVULA NDIPO  
AKUVINIRA FANO. NDIYENERA KULANGA  
ANTHU ONSEWO. MITIMA YAO NDI  
YOUMA. SACHITA CHILINGAMO."**




MOSE ANAKWIYA ATAONA KUTI ANTHU  
AIWALA MULLINGU PODZIPANGIRA FANO.

**MWASWA  
MALAMULO A  
MULLINGU.**



MOSE ANAPHWANYA  
MIYALA IMENE  
MALAMULO  
ANALEMBEDWAPO.



MILINGU INA KOMA  
YEHOVA YEKHA? KODI FANO,  
LIMENE MWAPANGA NDI  
MANJA ANU, NKUKHALA  
MLENGI WANU?

MOSE ANAPHWANYA FANO  
LAGOLIDE LAMWANAWANG'OMBE  
LIJA, NALIPERAPERA MPAKA  
KUKHALA FUMBI.

EKSODO 20:3-4, 32:15-20






NGATI MULI KU MBALI YA  
YEHOVA BWERANI KUNO MUIME  
NDI INE. KOMA NGATI MUFUNA  
KUMAPEMBEDZA MILLINGU YA  
AIGUPTO, KHALANI POMWE  
MULIPO.

TIDZATSATA  
MULLINGU WA  
ABRAHAMU,  
ISAKE, NDI  
YAKOBO.

NDI BWINO KUTI  
TITSATIRE MULLINGU  
AMENE ANAGAWA NYANJA  
YOFIIRA, NGAKHALE KUTI  
ALIBE CHIFANIZO.



CHILANGO CHA TCHIMO  
NDI IMFA. YEHOVA AKUTI  
ANTHUWA AYENERA KUFA BASI.  
TSOPANO TENGA LUPANGALAKO  
NDIPO UPHE ANTHU ONSE  
AMENE AMAGWIRITSA NTCHITO  
ZIFANIZO POPEMBEDZA.



ANTHU 3,000  
OPEMBEDZA MAFANO  
NDI ACHIGOLOLO  
ANAPHEDWA PA TSIKU  
LIMENELO.

**KHAAAAA!**

**MAYOOO!**

**CHITIRENI  
CHISONI!**


**EKSODO 32:26-28**



MOSE ANAKWERA PHIRI, NDIPO  
MULINGU ANALEMBANSO MALAMULO  
KHUMI AJA PA MIYALA IWIRI. MOSE  
ATATSIKA PHIRILO, ANAONETSA  
ANTHU MALAMULO A MULINGU,  
NDIPO ONSE ANAVOMEREZANA ZOTI  
ADZAMVERA MALAMULOWO.




MULLINGU AKUTI INU NDINU A  
MTIMA WOLIMA NDIPONSO OUKIRA.  
MUTACHIMWA PAJA, ADANDIENZA KUTI  
ADAFUNA KUKUPHANI NONSENU,  
KOMA NDINAKUPEMPHERERANI, NDIPO  
ADZAKUKHULULUKIRANI. YEHOVA NDI  
WACHIFUNDO NDIPONSO  
AMAKHULULLUKA.



MULLINGU WANDIENZA MMENE TIMANGIRE  
HEMA LOPATULIKA. TIKALIMANGA MONGA IYE  
WANENERA, ADZAKUMANA NAFE KOMWEKO.  
POPEZA TONSEFE NDIFE OCHIMWA, MULLINGU  
WAKONZA NJIRA IMENE TINGAMUYANDIKIRIRE.

ALEVI AZIDZAPEREKA NSEMBE TSIKU  
NDI TSIKU. KAMODZI PA CHAKA CHILICHONSE,  
MAGAZI AZIDZAPAKIDWA PA BOKOSI LA  
CHIPANGALO. MULLINGU AKAONA MAGAZIWO PA  
BOKOSI LA CHIPANGANOLO, MONGA ANACHITIRA  
KU IGUPTO, ADZATIKHULLULUKIRA, NDIPO  
SITIDZAFI. IYI NDI NJIRA IMENE MULLINGU  
ADZATIKHULLULUKIRIRE MACHIMO ATHU.



HEMA LOPATULIKA LIJA  
LINAPANGIDWA, NDIPO ANSEMBE  
ANAYAMBA KUPEREKA NSEMBE  
TSIKU NDI TSIKU. MULLINGU,  
AKAONA CHIKHULUPIRIRO CHA  
ANTHU AMENE ANKAPEREKA  
MAGAZI A NYAMA,  
ANKAKHULLULUKIRA MACHIMO AO.

KOMA ANTHU  
SANKAKONDWA CHIFUKWA  
CHOKHALA M'CHIPULULU,  
CHONCHO ANKADANDAULA  
NTHAWI ZONSE.

TSIKU LINAFIKA, NDIPO  
KUDANDAULA NDI  
KUSAKHULUPIRIKA KWAO  
KUNACHITITSA KUTI  
MULLINGU AWALANGE.



**EEEE! ONANI!  
NJOKA...  
ZAMBIRITU!**

MULLINGU ANABWERETSA NJOKA  
ZALLULU ZAMBIRI PAKATI PAO  
KUTI ZIWALUME. INDE,  
MULLINGU NDI WACHIFUNDO  
KOMA SALEKERERA TCHIMO.

**EKSODO 34:28-32, 39:32; NUMERI 21:5-6**





POSAKHALITSA  
MSASA WONSE  
UNADZAZA NDI  
NJOKA ZAULULU.



**TITHANDIZE  
NI  
MULLINGU!**

NJOKA ZINKAWAPEZA  
NGAKHALE M'MAHEMA  
MWAO USIKU.

SIIIIII





THANDIZENI.  
NDALUMIDWA.



**AIIIIII!**


**AI, EBENI!**

**AMAI!**



**NGAKHALE ANA  
ANAZUNZIKA CHIFUKWA  
CHA KUCHIMWA KWA  
MAKOLO AO.**

**NUMERI 21:6**



MUMSASA MONSE, KULIRA  
KOSONYEZA KUZUNZIKA NDI  
KUDANDAULA KUNAMVEKA.  
MALIPIRO A LICHIMO NDI  
OWAWA KWAMBIRI.

MUMSASA MONSE  
ZINTHU ZAFIKA  
PAMENEPA NDIPO  
ZIPYOLABE APA. ANTHU  
AMBIRI AFA KALE.

TIFUNEFUNE KOMWE  
KULI MOSE BASI. ZIMENEZI  
AKUCHITA NDI MULLINGU.  
WAKWIYA CHIFUKWA CHA  
MACHIMO A ANTHUWA.

**TCHAAA!**



UYANKHULE NDI MULLINGU.  
INDE TIYENERA KULANGIDWA,  
KOMA UMUPEMPHE KUTI  
ATICHITIRE CHIFUNDO.

KODI ANTHU  
ADZAZINDIKIRA LITI  
KUTI MULLINGU AMADANA  
NDI TCHIMO? AYENERA  
KUMVERA MALAMULO AKE  
NDI KUKHALA ANTHU  
OPATULIKA.



A man with curly hair, wearing a brown robe, is shown in a state of deep prayer, bowing his head and torso towards the ground. His hands are clasped together in front of him. The background is a simple, light-colored wall with some faint lines suggesting a room or outdoor setting.

MULLUNGU, CHONDE  
CHITIRANI CHIFUNDO  
ANTHU ANU.  
AKHULLULUKIRENI.

*PITA. KAPANGE  
NJOKA YAMKLIWA,  
YOFANANA NDI ZIMENE  
ZIKULLUMA ANTHU. UYIIKE  
PAMTENGO POTI ANTHU  
ONSE ATHA KUYIONA.  
UWALUZE KUTI  
AZINGOYANG'ANA NJOKA  
YAMKLIWAYO, NDIPO  
ADZACHIRA NTHAWI  
YOMWEYO.*

MULLINGU WAKONZA  
NJIRA. MUNGOPYANG'ANA  
NJOKA YAMKUWAYO, NDIPO  
MUDZACHIRITSIDWA.





AFA  
BASI.

**AI!** MULLINGU  
WAKONZA NJIRA.  
TANGOTSEKULANI  
MASO ANUWO,  
YANG'ANANI.  
YANG'ANANI KUTI  
MUKHALE NDI  
MOYO.



**NCHOZIZ  
WITSA!**

**TIYENERA  
TIUZEKO  
ANZATHU.**

**AI! MULLINGU  
WAKONZA NJIRA.  
TANGOTSEKULANI  
MASO ANUWO,  
YANG'ANANI.  
YANG'ANANI KUTI  
MUKHALE NDI  
MOYO.**



**YANG'ANANI  
KUTI MUKHALE  
NDI MOYO!**

**NUMERI 21:9**



NCHIFUKWA CHIYANI  
LKUMUNAMIZA?

ENATU  
ANAYANG'ANA  
NDIPO  
ACHIRITSIDWA.

KODI SUKUONA  
KUTI NDIKUFU? BWANJI  
LKUNDIVUTITSA NDI  
BODZA LAKOLO?



WAMWALIRA.

SANAKHULLUPIRIRE.

ANALI  
WONYADA,  
WOSAFUNA  
KUMVA ZA  
ANZAKE.


PA NTHAWI IYINSO ANTHU ANAONA  
MPHAMVU ZA MULLINGU. ANASAMUTSA  
MSASA KUCHOKA KUMENE KUNALI  
NJOKA KUJA NDIPO ZINTHU  
ZINAYAMBANSO KUYENDA BWINO.



KOMA ANTHUWO  
ANAPITIRIRABE KUCHIMWA,  
KAWIRIKAWIRI SANKAMVERA  
MALAMULO A MULLINGU.








AISRAELE ANALONDOLABE MTAMBO  
UJA. MULLINGU ANAWADYETSA MANA  
KUCHOKERA KUMWAMBA NDIPO  
ANKAWAPATSANSO MADZI AKUMWA.

AKADAWATSOGOLERA MPAKA KU DZIKO  
LAMALONJEZANO, KOMA ANALI OSAMVERA NDIPO  
SANKATSATIRA MALAMULO AKE, CHONCHO MULLINGU  
ANAWAYENDE TSA M'CHIPULULU KWA ZAKA 40.

NUMBERS 21:9, 32:13

MOSE, UMAGANIZA KUTI IWE WEKHA NDIYE UKHOZA KUYANDIKIRA KWA MULLINGU. IFENSO NDIFE OYERA MONGA MMENE ULILI IWEYO. ZOONA ZAKE NZAKUTI, ANTHU ONSEWA NDI OYERA. TSOPANO PALIBE OCHIMWA PAKATI PATHU, NDIPO MULLINGU AMAKHALA PAKATI PATHU. SITIKUFUNA KUTI IWEYO NDI AARONI MUZITUZA ZOYENERA KUCHITA, SITIKUFUNANSO KUTI MUKHALE OTIWERUZA. IFENSO TIKHOZA KUMAWERUZA MONGA INU NOMWE.




AAAA, NDATOPA NDI KUMANGOYENDA M'CHIPULULU MUNO, NDIPO MULLINGU AKUNGOTIPHA PA ZIFUKWA ZOSAKWANIRA.

INDE, MOSE NDIYE ANALAKWA. KAYA AMAYEMBEZEZA KUTI TIZICHITA MOTANI?

MOSE ANAPITA M'HEMA  
LOPATULIKA KUKAMFUNSA  
MULUNGU ZOTI ACHITE.






**MULLINGU AKUTI,  
"MUKUDZISENZETSA NOKHA  
MAUDINDO, INU ANA A LEVI.  
ZIKANAKHALA BWINO KUTI ANTHU  
ANU AKHALE ANSEMBE  
OSANKHIDWA NDI MULLINGU.**

**MAWA AMBUYE ADZAWERUZA  
PAKATI PATHU, NDIPO TIDZADZIWA KUTI  
ANSEMBE ENIENI A MULLINGU WOYERA NDANI,  
NDIPONSO KUTI ANSEMBE ABODZA NDANI.  
MUBWERE KU HEMA LOPATULIKA MAWA  
MMAWA. MUKABWERETSE ZOFUKIZIRA  
LUBANI NDI MOTO MMENEMO.**

**NUMERI 16:2-6**

# MMAWA UJA WAFIKA



SENDERANI PAFUPI,  
INU AMENE MUMATI NDINU  
WOYERA, MUMATI NDINU  
OYENERA KUKHALA ANSEMBE  
NDI OWERUZA ANTHU.

MULUNGU AKUMANA NAFE  
LERO, NDIPO ASANKHA YEKHA.  
TIDZAONA MPHAMVU ZAKE  
ZAZIKULU KOMANSO  
ULEMERERO WAKE.



**DZIPATULENI NOKHA  
KWA ANTHU OIPAWA.  
NDIKUFUNA KUWAPHA  
TSOPANO.**




**MUTULUKE  
M'MAHEMA MWAO.  
MUSAWAYANDIKIRE KUTI  
MUNGAFE NAWO  
PAMODZI.**





NKHANI ILI MOTERE: NGATI ANTHU AWA ADZAFANA NDIMFA YA CHILENGEDWE, MUDZAZINDIKIRA KUTI NDINE MNENERI WABODZA NDIPO KUTI MULLINGU SAYANKHULANANE.



KOMA LERO MUKAONA CHINTHU CHACHILENDO, NGATI NTHAKA ING'AMBIKA NDI KUMEZA ANTHU AMENEWA PAMODZI NDI ZAO ZONSE NDI KUPITA NAWO KUDZENJE LACHIONONGEKO, PAMENEPO MUDZAZINDIKIRA KUTI ACHIMWIRA MULLINGU NDIPO KUTI INE NDIYE MNENERI WAKE.



**THANDIZENI!**


**IIIIII!**

**MAYOOOO!**

ANTHU ONSE AMENE ANKADZIYESA KUTI  
NDI ANSEMBE ANAMEZEDWA AMOYO  
M'MOTO WA KU GEHENA UMENE  
UNAKONZEDWERA SATANA NDI ANGELO AKE.




NUMERI 16:28-33



ANA A ISRAELE  
SAKANAIWALA  
TSIKU LIMENELO.  
MULINGU  
ANAONETSA KUTI  
MOSE NDIYE  
ANALI MNENERI  
WAKE, NDIPO  
OKHAWO AMENE IYE  
WASANKHA NDIWO  
ANKAYENERA  
KUKHALA ANSEMBE.

TENGANI  
ZOFUKIZIRA LUBANI  
ZAO ZAMKUWA NDIPO  
MUZIGWIRITSE  
NTCHITO POPANGIRA  
CHOTCHINGIRA GUWA  
LA NSEMBE.

MUKADZAONA CHOTCHINGIRA  
GUWA CHAMKUWA  
MUZIDZAKUMBUKIRA TSIKU  
LIMENELI, PAMENE ANTHU  
ANANYOZERA MALAMULO A  
MULINGU NAFUNA KUDZIIKA PA  
UDINDO WA UNSEMBE.




ULEMERERO WA  
MULLINGU ULI NAFE  
NDIPO AKUTIPATSA  
MKATE KUCHOKERA  
KUMWAMBA.

ULEMERERO WA MULLINGU UNKAKHALA PA  
HEMA LOPATULIKALO NTHAWI ZONSE NDIPO  
AISRAELE ANKATSATIRA MOSE KULIKONSE  
M'CHIPULULU MUJA KWA ZAKA 40.

MULLINGU ANKAWAGWETSERABE MKATE  
KUCHOKERA KUMWAMBA NDIPO ANKAWAPATSA  
MADZI KUCHOKERA M'MWALA. MOTO  
UNKAWAKUTA USIKU NDIPO MTAMBO  
UNKAWAKUTA USANA. ANAKHAZIKIKA NDIPO  
ANAPHUNZIRA KUSUNGA MALAMULO A MULLINGU.

NUMERI 16:37-38



ANSEMBE ANKAKHALA  
KU HEMA LOPATULIKA  
NDIPO ANKAPEREKA  
NSEMBE ZA TSIKU NDI  
TSIKU MONGA MOMWE  
MOSE ANALAMULIRA.



PATAPITA ZAKA 40, NTHAWI IMENE ANTHU ANKAYEMBEZERA KULOWA M'DZIKO LAMALONJEZANO, MULLINGU ANALIZA MOSE KUTI APITE KU PHIRI KUKAKUMANA NAYE. KUMENEKO, ATATHA KUKAMBIRANA NDI MULLINGU, ANAKHALA PANSI NDIPO ANAMWALIRA.



MWANSANGAMSANGA, MZIMU WAKE  
UNAPITA M'MANJA MWA MULLINGU.  
KUMENEGO NDIKO AKUKHALA MPAKA  
PA CHIMALIZIRO CHA NTHAWI  
PAMENE ADZALONDOLA ANTHU AKE  
KU DZIKO LIMENE MULLINGU  
ANALONJEZA ABRAHAMU.

PAFUPIFUPI 1451 B.C. - DEUTERONOMO 34:4-5




PANAPITA PAFUPIFUPI ZAKA 500  
KUCHOKERA PAMENE MULLINGU  
ADAALIZA ABRAHAMU KUTI ACHOKE  
M'DZIKO LA KWAO NDI KUPITA KU DZIKO  
LIMENE MULLINGU ADZAMPATSE.

LONJEZO LA MULLINGU  
KWA ABRAHAMU NDI  
SARA, LOTI ADZAKHALA  
MTUNDU WAUKULU  
KUPYOLERA MWA ISAKE,  
LINAKWANIRITSIDWA. ANA  
12 A YAKOBO, AMENE  
DZINA LAKE  
LINASINTHIDWA KUKHALA  
ISRAELE, ANALI MAFUKO  
12 NDIPODI UNALI  
MTUNDU WAUKULU WA  
ANTHU.






ANACHOKERA KU UKAPOLO, ANAYENDA  
M'CHIPULULU NDI MOSE, ANALANDIRA MALAMULO A  
MULUNGU, NDIPO TSOPANO ANALI PAFUPI KULOWA  
M'DZIKO LAMALONJEZANO. PA ULENDU WONSE WA  
M'CHIPULULU, MNYAMATA WINA ANKAKHALA NDI  
MOSE NTHAWI ZONSE, AMAONA NDI KUPHUNZIRA  
ZA KAYENDETSEDWE KA MTUNDU WA ISRAELE.



MNYAMATA AMENEYO  
ATAKULA, ANAKHALA MSILIKALI  
WAMPHAMVU KWAMBIRI; DZINA  
LAKE NDILO YOSWA.

MOSE ATAPITA KUKAKHALA NDI  
MULLINGU, MULLINGU  
ANASANKHA YOSWA KUTI  
ATSOGOLERE ANTHUWO KUPITA  
NAWO M'DZIKO LIMENE  
ADAALONJEZA ABRAHAMU.



ANTHUWO ADAKUMBUKA LINENERI WAKUTI  
ADZAKHALA ALENDO M'DZIKO LA ENI, NDIPO KUTI  
PAKADZAPITA ZAKA 400 MULLINGU  
ADZAWATULUTSA NDI KUWABWEZERA KU DZIKO  
LIMENE MULLINGU ANALONJEZA MAKOLO AO.  
MULLINGU ANASUNGA MAU AKE.

PA TSIKU LIMENE ANAOLOKA  
YORDANO, MANA ANALEKA KUGWA  
KUCHOKERA KUMWAMBA NDIPO  
ANKADYA ZAKUDYA ZA M'DZIKOLO.

AMUNA  
ANGA, DZIKO  
LIMENE MULINGU  
WATIPATSALI NDI  
LOKONGOLADI.

DEUTERONOMO  
34:9; YOSWA 5:12

INDE, NDI DZIKO  
LABWINO LOTI  
TILEREREMO ANA NDI  
KUWAPHUNZITSA ZA  
MOYO WOPATULIKA NDI  
WA MTENDERE.





<https://goodandevilbook.com/>